# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

## Momwe Mulungu asamalira ndi kuthandiza anthu onse, koma makamaka ana ake


1. Mulungu anapatsa Mwana wake cifukwa ca ife
2. Mulungu amatisamalira
3. Mulungu asandutsa mabvuto athu kuti mabvuto atipindulitsa
4. Angelo a Mulungu atilondera
5. Mulungu afuna kuti ndife okondwa
6. Tifunika thandizo kukhala miyoyo yathu kwa Mulungu
7. Atate atithandiza pamene timpempha
8. Mzimu Woyera atithandiza
9. Yesu atipempherera
10. Angelo atilondera


Nkokoma kuti munthu ayembekeze ndi kulindirira modekha cipulumutso ca Yehova – Maliro 3.26

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

**1. Mulungu anapatsa Mwana wake cifukwa ca ife**

*Pakuti mphoto yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu – Aroma 6.23*

**Kuwerenga**
Luka 2.8-18

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira phunziro la uchimo? Tinaphunzira kuti ife tonse ndife ocimwa ndipo ife tonse tiyenera kulangidwa. Mulungu amacita zoyenera ndipo macimo ayenera kulangidwa.
Koma Mulungu safuna kutilanga. Mulungu woyera atikondabe ngakhale ndife ocimwa kwambiri.
Mukumbukira kuti Mulungu anapulumutsa Nowa m'chombo. Nthanoyo iri yabwino kwambiri. Mulungu anakhala wabwino pali Nowa. Koma nthano yodabwitsa koposa m'dziko lonse lapansi ndiyo nthano ya momwe Mulungu apulumutsa anthu. Anatuma Mwana wake wobadwa yekha kuti Iye atenga cilango m'malo mwa ife. Mulungu analanga macimo athu pamene Yesu anafa pa mtanda. Ndipo tsono ngati timkhulupirira, sitiyenera kulangidwa konse cifukwa ca macimo athu!
Baibulo litiuza momwe Yesu anadza pa dziko lapansi ngati Mwana wakhanda wobadwa m'Betelehemu. Mariya mai wake anamuika modyera ng'ombe.
Pa mapiri kunja kwa Betelehemu, abusa ena anayang'anira nkhosa zao usiku womwewo. Mwadzidzidzi anaona kuwala kwakukulu. Kuwala kunacokera Kumwamba. Ndi mngelo wotsika pansi!
Abusa anamva kwambiri yaikulu. Koma mngelo anawauza, 'Musaope'. Anati, 'Ndikuuzani uthenga wabwino. Wakubadwirani m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi amene ali Kristu Ambuye!'
O, uthenga wabwino kwambiri! Kale kale Mulungu adalonjeza kutuma Mpulumutsi. Ndipo tsono Mpulumutsi anabadwa!
Kenaka abusa anaona makamu a angelo akuwala pa tambo la kumwamba. Angelo anaimba, 'Ulemerero ukhale kwa Mulungu!' Abusa anaima kumeneko nayang'ana ku mwamba namvera nyimbo yabwino. Kunalibe munthu amene adamva konse makamu otere a angelo.
Pamene angelo anabwerera Kumwamba, abusa anathamanga kupita ku Betelehemu. Kumeneko anaona Mpulumutsi: Yesu Mwana wakhanda. Ndipo anakondwa kwambirimbiri.
Yesu anakhala pa dziko lapansi zaka makumi atatu. Anacita zabwino zambiri. Anaciritsa anthu odwala. Anapenyetsa akhungu. Anapita paliponse kucita zabwino.
Ndipo kenaka anacita codabwitsa koposa. Anadzipereka kutifera pa mtanda. Anafa pa mtanda kulipira macimo onse. Anatenga cilango cimene tiyenera kukhala naco.
O, Mulungu ndi wabwino kwambiri! Atikonda kwambiri! Anatuma Mwana wake Yesu kutifera. Ndipo o, Yesu atikonda kwambiri! Anakhala wofuna kutifera pa mtanda.
Ndipo tsopano Mulungu apatsa moyo wosatha kwa iwo onse amene akhulupirira Yesu. Tidzakhala naye muyaya kumkonda, kumtumikira ndi kukhala osangalala nthawi zonse.

**Kukambirana**
1. Kodi Yesu anadza pa dziko lapansi kucita ciani?
2. Cifukwa ciani cikondi ca Mulungu ndi ca Yesu ndico codabwitsa?
3. Kodi Yesu anakhululukiranso macimo anu? Cifukwa ciani mwayankha tero?
4. Mulungu akamba kuti, 'Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo' (Macitidwe 4.12). Kodi ndime iyi itanthauza ciani?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Tikuyamikani kuti munatuma Mwana wanu Yesu pa dziko lapansi. Cifukwa ca Iye tikhoza kukhululukidwa ku macimo athu onse. Tikuyamikani kaamba ka cikondi canu. Mudziwa momwe tikhala pa maso panu. Tikupemphani kuti mutikhululukire macimo athu onse. M'dzina la Yesu Mpulumutsi tikupemphani. Amen.

## 2. Mulungu atisamalira

*Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa – Salimo 23.1*

**Kuwerenga**
Salimo 23

**Malongosoledwe**
Mulungu atikonda kwambiri. Anaonetsa cikondi cace cacikulu potipatsa Yesu Mwana wake wokondedwa kutifera. Indedi, ngati atikonda kotero, adzatisamalira nthawi zonse, si m'mene?
Baibulo likamba kuti Mulungu adzatisamalira nthawi zonse. Baibulo litiuza kuti atisamalira m'zonse zimene zingacitike. Pa nthawi ya tsiku ndi usiku, masiku alionse ndi usiku wonse; Iye atisamalira.
Kodi mukumbukira Davide, mnyamata wowetera nkhosa amene anasanduka mfumu yaikulu? Davide anakonda Mulungu. Ndipo Davide anadziwa kuti Mulungu amkonda. Davide analemba nyimbo zambiri (masalimo). Nyimbo zina zipezeka m'Baibulo. Nyimbo imodzi ichedwa 'Salimo la mbusa'.
Pamene Davide anali mnyamata wowetera nkhosa, iye anasamalira bwino nkhosa zake. Anazipezera udzu kuti zidye. Anazisogolera ku madzi abwino kuti zimwe. Pamene kunatentha kwambiri, anazipezera malo a mthunzi kuti zipumule. Anadikira kuona kuti tiana ta nkhosa sititsakamuka ku miyala yaikulu kapena kupweteka m'njira ina. Anadikira kuti cilombo cacikulu sicibwere kugwira nkhosa imodzi. Kusanade, iye anasonkhanitsa nkhosa zonse nazibweretsa m'khola. Momwemo nkhosa zinali zotetezeka. Kenaka Davide anakhala pansi pa citseko kuti kunalibe ciriconse comwe cingalowemo usiku kupweteka nkhosa. Davide anali mbusa wabwino kwambiri. Angapereke moyo wake ngati ciriconse cingabwere kugwira nkhosa.
Pamene Davide anaganizira njira yomwe asamalira nkhosa zake, iye anaganizira Ambuye Mulungu ndi momwe Iye amasamalira nkhosa zake. Ndipo analemba Salimo iri yoimba za Ambuye wosamalira nkhosa zake. Ndipo Davide anadziwa kuti anali m'modzi wa nkhosa za Ambuye. Ndipo anadziwa kuti Mulungu ndi Mbusa wabwino.
Tsiku lina Yesu anati kwa ophunzira ake, 'Ine ndine Mbusa wabwino'.
Inde, Ambuye Yesu ndi Mbusa wabwino kwambiri, Mbusa wapadera kwambiri. Atiyang'anira nthawi zonse ndipo Iye sagona konse.
Kodi nkhosa za Yesu ndizo yani? Mudziwa yankho?
Inde, anthu onse a Mulungu ndiwo nkhosa za Yesu. Yesu awasamalira, monga Davide anasamalira nkhosa zake. Anyamata ndi atsikana ndiwo tiana ta nkhosa ta Yesu. Yesu awakonda. Awayang'anira monga Davide anayang'anira tiana ta nkhosa take. Mulungu atikonda. Atisamalira.
Pamene tikumbukira kuti atikonda, tingakondwere tingakhale kudwala. Tingakondwere pa nthawi ya mabvuto. Tingakondwere ngakhale pa nthawi ya imfa yathu. Kumwamba tidzaona Mbusa Wabwino.

**Kukambirana**
1. Kodi Mbusa wabwino amacita ciani?
2. Ambuye Yesu anati, 'Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wace cifukwa ca nkhosa' (Yohane 10.11) Citanthauzanji kuti Yesu anataya moyo wace cifukwa ca nkhosa?
3. 1 Petro 2.25 ikamba kuti, 'Pakuti munali kusocera ngati nkhosa; koma tsopano mwabwera kwa Mbusa ndi Woyang'anira wa moyo wanu'. Nanga inu, munalapa ku macimo anu ndi kupita kwa Ambuye Yesu kupeza cipulumutso mwa Iye?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, Inu ndinu Mbusa wabwino. Tikuyamikani kuti mumasamalira nkhosa zanu. Nthawi zambiri ticoka kwa Inu, ndife otayika cifukwa ca macimo athu. Mutibweretse pafupi nanu mwa mphamvu yanu. Tikupemphani m'dzina lanu, Amen.

## 3. Mulungu asandutsa mabvuto athu kuti mabvuto atipindulitsa

*Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kusimikiza kwa mtima wace – Aroma 8.28*

**Kuwerenga**
Genesis 45.1-8

**Malongosoledwe**
Ngati Mulungu atikonda ndi kutisamalira, cifukwa ciani kuli mabvuto? Ana a Mulungu angadwale nthawi zina. Ali ndi mabvuto ndiponso kuwawa. Ngakhale tiana ta nkhosa ta Mulungu tingadwale nthawi zina kapena kupweteka. Pamene kuli mabvuto, Mulungu aiwala kutisamalira kodi?
O, iai! Masautso atipindulitsa. Ici ndi cinthu codabwitsa, iai? Kodi mabvuto atipindulitsa bwanji?
Baibulo litiuza nthano yodabwitsa ya mnyamata wochedwa Yosefe. Anali ndi mabvuto ambiri. Koma mabvuto ake onse anasanduka kukhala ubwino wake ndi wa anthu ena ambiri a Mulungu.
Yosefe anali ndi abale ake khumi. Iwo sanali anyamata abwino nthawi zina. Nthawi zina anacita zoipa. Yosefe anali mnyamata wabwino. Inde, m'mtima mwake munalinso uchimo. Koma anayesa kucita zabwino. Yakobo tate wake anakonda kwambiri Yosefe.
Nthawi zina Yosefe anauza tate wake zoipa zimene abale ake adacita. Ici cinakalipitsa abale ake. Patapita nthawi iwo anada Yosefe.
Tsiku lina Yakobo anatuma Yosefe kuona momwe abale analiri. Iwo anali kutali. Adapita kutali kupeza msipu wabwino kukawetera nkhosa zao. Yosefe anapita kuwapeza.
Abale anaona Yosefe kubwera. Ananena wina ndi mnzace, 'Tiyeni ticotse Yosefe!'
Kotero, pamene Yosefe anabwera pafupi, iwo anamgwira. Anamuponya m'dzenje lakuda. Yosefe analira. Anati, 'Conde, ndicotsemo! Ndiloleni kupita kunyumba!' Koma abale sanamvere.
Patapita nthawi kunabwera amuna oyenda pa ngamira. Abale a Yosefe anati, 'Tigulitse Yosefe kwa amunawa. Adzamtenga kutali. Kotero sitidzamuonanso konse. Tidzamcotsadi ndipo tidzauza tate wathu kuti cilombo cidamupha Yosefe.'
Anagulitsa Yosefe. Ndipo anauza Yakobo tate wao kuti cilombo cidamupha. Koma amuna anatenga Yosefe ku Aigupto. Yosefe anasanduka kapolo m'Aigupto.
Zaka zinapita. Kunali njala. Kunalibe cakudya. Kunalibe mvula. Mbeu sizinakule. Abale a Yosefe analibe buledi kudyetsa mabanja ao.
Tsiku lina Yakobo anati kwa ana amuna ake, 'Ndamva kuti kuli buledi ku Aigupto. Pitakoni kukagula'. Ndiye abale anapita.
M'Aigupto analankhula ndi nduna ya mfumu. Nduna analankhula nao mokalipa. Anati kuti ndiwo akuba ndi azonda. Anaika ngakhale m'modzi wao m'ndende.
Abale anati, 'Ici ndi cifukwa tidagulitsa Yosefe! Mulungu atilanga'. Anaopa.
Koma ndunayo ndiyo Yosefe ndipo patapita nthawi anawauza kuti iye ndi Yosefe, mbale wao. Iwo anadabwa kwambiri!
Yosefe anati, 'Osacita mantha. Sindidzakulangani. Mudacita zoipa koma Mulungu anazisandutsa zabwino kuti tikhale ndi mbeu zokwanira kudyetsa ife tonse pa nthawi iyi ya njala'.
Mabvuto onse a Yosefe anasaduka ubwino wake ndi wa anthu a Mulungu. Tiyenera kukhulupirira kuti mabvuto athu *onse* atipindulitsa, pakuti Mulungu atikonda. Salola ciriconse kucitika cimene sicitipindulitsa.

**Kukambirana**
1. Kodi tiona bwanji m'nthano ya Yosefe kuti Mulungu alamulira zonse?
2. Cifukwa ciani Mulungu alola anthu ake kubvutika?
3. Kodi tiloledwa kudandaula?
4. Tiyenera kucita ciani pa nthawi ya masautso?
5. Werenganinso Aroma 8.28. Kodi mumakonda Mulungu pansi pa mtima wanu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Muli ndi mphamvu zonse. Mukhoza kusandutsa mabvuto kotero kuti atipindulitsa. Nthawi zambiri sitimvetsa ulamuliro wanu. Nthawi zambiri tidandaula. Tiphunzitseni kukukhulupirirani nthawi zonse. Tikuyamikani kuti mutiphunzitsa mogwiritsa nchito mabvuto amene tikomana nao. Tithandizani kukulemekezani m'zonse zimene zicitika. Tikupemphani zonse mwa cisomo, m'dzina la Yesu, Amen.

## 4. Angelo a Mulungu atilondera

*Pakuti adzalamulira angelo ace za iwe – Salimo 91.11a*

**Kuwerenga**
Danieli 6.16-23

**Malongosoledwe**
Mafumu onse ali ndi atumiki. Atumiki acita ciriconse cimene mafumu ao awauza kucita. Apita kulikonse komwe mafumu awauza kupita.
Mulungu ndi Mfumu wopambana. Iye ndi Mfumu wa pa dziko lonse lapansi komanso wa kumwamba. Ndipo ali ndi makamu a atumiki. Atumiki a Mulungu ndiwo angelo oyera ndi odabwitsa.
Mulungu anapanga angelo kale kale, Iye asanalenge Adamu ndi Hava. Iwo ndiwo atumiki ake ndipo akondwera. Amlemekeza Mulungu ndipo acita ciriconse cimene Iye awauza kucita.
Sitiona konse angelo. Sitikhoza kuwaona cifukwa iwo ndi mizimu. Koma tidziwa kuti Mulungu awatuma pa dziko lapansi kutilondera ndi kutithandiza. Iwo alowa m'nyumba zathu, m'macalichi ndi m'masukulu. Apita kulikonse komwe Mulungu awatuma kucita zimene Iye afuna iwo kucita.
Baibulo litiuza za mwamuna wolimba mtima wochedwa Danieli. Danieli analimba mtima kupempha Mulungu ngakhale mfumu wa Babulo adanena kuti Danieli saloledwa kupemphera. Danieli anakonda Mulungu.
Mfumu anapanga lamulo lonena, 'Masiku makumi atatu munthu aliyense saloledwa kupempha Mulungu wake. Aloledwa kundipempha zosowa zake kwa ine, mfumu wa Babulo. Ngati munthu apempha Mulungu wake, iye adzaponyedwa m'dzenje la mikango.'
Danieli ankagwada pansi kupempha Mulungu katatu tsiku lirilonse. Danieli atamva lamulo latsopano, iye anapita kunyumba nagwada pansi monga ankacita nthawi zonse.
Mazenera a nyumba ya Danieli sanabvalike. Amuna ena anamuona kugwada pansi kupemphera. Iwo anada Danieli. Anathamanga kuuza mfumu kuti Danieli samvera lamulo latsopano. Anafuna mfumu kuponya Danieli m'dzenje la mikango.
Iwo anati, 'O mfumu, mudziwa lamulo latsopano. Masiku makumi atatu palibe munthu wina aliyense wololedwa kupempha Mulungu wake. Ngati munthu apempha Mulungu wake, ayenera kuponyedwa m'dzenje la mikango. Cabwino, taona Danieli ali kugwada pansi kupempha Mulungu wake!'
Pomvera uthenga uja, Mfumu anamva cisoni. Anakonda Danieli. Koma sanakhoze kulola munthu kusamvera lamulo lake. Ndiye anatuma anthu kugwira Danieli. Ndipo anauza atumiki ake kuponya Danieli m'dzenje la mikango.
Danieli abvutika! Pamene amuna anamponyamo, iye anagwa munsi m'dzenje la mikango. Mikango inathamanga kumng'amba.
Koma… mikango sinamng'ambe Danieli! Sinakhoze. Inali ndi njala. Inafuna kudya Danieli. Koma Mulungu anatuma mngelo kusunga mikango patali pa Danieli. Mikango sinakhoze ngakhale kutsegula pakamwa pao kuti ingadye Danieli.
M'mawa mfumu anayang'ana munsi m'dzenje. Anapfuula, 'Danieli, Mulungu anakhoza kukupulumutsani kodi?'
Danieli anayankha, 'Mulungu wanga anatuma mngelo wake kutseka pakamwa pa mikango'.
Mulungu atuma angelo kusamalira ana ake ngakhale lero. Sitikhoza kuona angelo, koma tidziwa kuti ali pafupi nafe cifukwa Baibulo akamba tero.

**Kukambirana**
1. Kodi udindo wa angelo ndiwo ciani?
2. Hebri 1.14 ikamba za angelo, 'Kodi siiri yonse mizimu yotumikira, yotumidwa kuti itumikire iwo amene adzalowa cipulumutso?' Nanga inu mudzalowa cipulumutso? Mwalandira Yesu kukhala Mbuye wanu kodi?
3. Kodi utumiki wa angelo utonthoza bwanji anthu oona a Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa makamu, Tikuyamikani kuti mutisamalira makamaka ana anu olapa ndi kulandira Yesu Kristu. Tiphunzitseni kukutumikirani monga angelo anu akutumikirani, kuti tizicita cifuniro canu nthawi zonse. Tikupemphani m'dzina la Yesu Mpulumutsi weniweni, Amen.

**5. Mulungu afuna kuti ndife okondwa**

*Ndidzakondwerera ndi kusekera mwa Inu; ndidzayimbira dzina lanu, Wam'mwamamwamba Inu – Salimo 9.2*

**Kuwerenga**
Salimo 100

**Malongosoledwe**
Kodi mwathokoza Mulungu lero pa zabwino zonse zimene akupatsani?
Akupatsani zinthu zabwino zambiri. Atipatsa madalitso ambiri tsiku ndi tsiku. Akupatsani anthu amene akukondani ndi kukusamalirani. Atipatsa nyumba zathu. Atipatsa cakudya cabwino ndi zina zonse zimene tifunika. Atipatsa zobvala zathu, zobvala zotitezezera mazizi kapena ngakhale zobvala zooneka bwino.
Nthawi zina Mulungu atipatsa kuwala kwa dzuwa. Nthawi zina atuma mvula. Dzuwa ndi mvula ndizo mphatso zabwino.
Mulungu analenga mbalame zimene zitiimbira. Analenga maluwa kusansuka ku malo athu, m'nkhalango ndiponso paliponse pa mbali za njira. Analenga dziko lapansi looneka bwino kutisangalatsa. Mulungu atulukitsa dzuwa m'mamawa onse. Nthawi zina apangitsa thambo kuoneka bwino pamene dzula lilowa. O, dziko lapansi ndi lodzala ndi mphatso zake zabwino.
Pamene Mulungu analenga Adamu ndi Hava, Iye anawaika m'munda wooneka bwino. Kunali zinthu zambiri zooneka bwino m'munda kuwakondweretsa. Koma Adamu ndi Hava anacimwa, monga mudziwa. Sanamvere Mulungu. Kenaka Mulungu anakhoza kuwauza 'Simuyenera kukhala ndi zinthu zooneka bwino. Ndidzakucotserani zinthu zonse zooneka bwino'. Koma Mulungu sanalankhule tero.
O inde, anacotsa Adamu ndi Hava m'munda. Ndipo anawauza kuti ayenera kugwira nchito molimba. Anawauza kuti kudzakhala mbeu zosafunika ndiponso minga zimene zidzawabvutitsa. Anawauza kuti iwo adzakhala ndi cisoni ndi kuwawa. Koma Mulungu anasiya zinthu zambiri zabwino ndi zokondweretsa kwa iwo kuti anakhoza kukondwerabe pang'ono. O, Mulungu anali wabwino kwa iwo. Ndipo Mulungu ndi wabwino kwa ifenso. Atipatsa zinthu zambiri kutikondweretsa.
Cifukwa ciani Mulungu atipatsa zinthu zambiri zabwino? Pakuti Mulungu atikonda. Tingakhale kumcimwirabe tsiku ndi tsiku, Iye atikonda mosasinthika. Tidziwa kuti atikonda, pakuti atipatsa zinthu izo zambiri kutikondweretsa ndiponso kuti moyo uli bwino kwa ife.
Pamene tiganiza za zonse zimene Mulungu atipatsa, tifuna kumkonda kwambirimbiri. Tifuna kumyamikira ndi kumlemekeza. Mulungu afuna kuti tizimyamikira ndi kuzimlemekeza. Afuna kuti tizimkonda. Akondwa ndi kusangalala pamene timkonda.
Cimwemwe ceniceni ciripo cabe pamene tiyesa kusangalatsa Mulungu ndi kumkonda koposa.

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu amatipatsa ciani?
2. Kodi mukumva bwanji za mphatso zocokera kwa Mulungu?
3. Kodi tingalemekeze Mulungu m'njira zotani?
4. Kodi cimwemwe ceniceni cicokera kuti?
5. Ambuye Yesu ananena, 'Comweco, ndinena kwa inu, kuli cimwemwe pamaso pa angelo a Mulungu cifukwa ca munthu wocimwa mmodzi amene atembenuka mtima'. Kodi angelo a Kumwamba akondweranso cifukwa ca inu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wakumwambamwamba, Cimwemwe ceniceni cicokera kwa Inu. Tikuyamikani kuti mufuna kuti tikondwera. Tikupemphani kuti mutipulumutsa ndi kutibweretsa pafupi nanu, kuti tikondwere ndithu. Tithandizeni kuzindikira kuti zabwino zonse zicokera kwa Inu. Zikomo kwambiri kuti mutipatsa zabwino zambiri tingakhale kukucimwirani. Cifundo canu ndi cacikulu! M'dzina lanu tikuyamikani ndi kupempha izi. Amen.

## 6. Tifunika thandizo kukhala miyoyo yathu kwa Mulungu

*Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi – 1 Yohane 1.8*

**Kuwerenga**
1 Yohane 1.7-2.1

**Malongosoledwe**
Nthawi zina azimai atiuza, 'Tsopano ndiyembekeza kuti mudzakhala atsikana abwino kapena anyamata abwino'.
Muwayankha kuti mudzacita bwino. Ndipo mufuna kucita bwino. Koma o, nthawi zina zambiri musamvera ngakhale poyamba mudafuna kumvera.
Ndipo nthawi zina mufuna ngakhale kusamvera!
Ngati ndife ana a Mulungu, Iye atiyembekezera kukhala abwino.
Mulungu atiuza, 'Muzindikonda koposa'. Ndipo anenanso, 'Muzikonda anthu ena monga inu mwini'. Koma nthawi zambiri tiiwala kukonda Mulungu koposa. Ndife odzikonda! Tidzikonda koposa, m'malo mwa kukonda anthu ena monga tidzikonda mwini.
Mulungu anena kuti sitiloledwa kunena mabodza, sitiloledwa kukalipa, kukwiya kapena kukhala osamvera. Koma ticita zinthu izi. O, nthawi zambiri!
Ngakhale Paulo, mtumiki wamkulu, sanacite bwino nthawi zina. Ndipo mfumu Davide wokonda Mulungu kwambiri, sanacite bwino nthawi zina.
Kulibe amene amacita zabwino nthawi zonse. Cifukwa ciani kukhala abwino ndi kobvuta kwambiri?
Ndi cinthu cobvuta cifukwa uchimo ndi wamphamvu, ngakhale ngati tiri ndi mtima watsopano. Mitima yathu ndi yodzala ndi mbeu za uchimo ndipo zimakula msanga kwambiri! Ndizo monga mbeu zosayenera.
Kodi muthandiza azimai anu kucotsa comera cosafunika m'munda? Mungacotse lero comera cosafunika conse, koma m'mawa comera cina cosayenera cidzakula. Kodi cicokera kuti? Cicokera m'mbeu zimene ziri m'nthaka.
Mbeu za macimo ziri m'mitima yathu. Ndipo zipitiriza kumera. Yesu akhululukira macimo athu pamene timpempha tsiku lirilonse, koma tsiku la m'mawa ticimwanso. Ngakhale ngati tiri ndi mitima yatsopano, mbeu za macimo ziyesa kukula. Sitikhoza kukhala abwino nthawi zonse.
Ici ndi cinthu cacisoni. Tizikhala miyoyo yathu kwa Mulungu ndi kumlemekeza, koma sitikhoza. Nthawi zina sitifuna. Kusafuna ndi comera cosafunika coipa koposa.
Paulo, mtumiki wamkulu, pamene analembera kalata anzake a ku Roma, iye anawauza kuti anamva cisoni cacikulu poganizira macimo opitiriza kumera m'mtima mwake. Anati, 'Sindifuna kucimwa, komabe ndicimwa'.
Petro amene anali wolimba mtima napitiriza kuuza za Yesu angakhale adaikidwa m'ndende, iye anadziwa kuti macimo anakula m'mtima mwake.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani kukhala abwino pa maso pa Mulungu si kotekha?
2. Ngati sitikhoza kukhala abwino pa maso pa Mulungu mwa mphamvu yathu, tifuna Yesu kutikonza kukhala abwino. Fotokozani njira momwe Yesu ndi Mpulumutsi.
3. Patsani zitsanso zitatu za comera cosafunika ca m'mtima mwanu.
4. Kodi mukumva bwanji za comera cosafunika m'mtima mwanu?

**Citsanzo ca pemphero**
Tikuyamikani Ambuye Yesu Kristu kuti mukhoza ndi kufuna konse kupulumutsa. Masiku onse tikucimwirani. M'mitima yathu muli mbeu zoipa zimene zibereka macimo. Tikhululukireni. Tipatseni Mzimu wanu Woyera kuti akhale m'mitima yathu kucotsa mbeu zoipa. Tikupemphani m'dzina lanu, Amen.

## 7. Atate atithandiza pamene timpempha

*Pemphani ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza – Mateyu 7.7a*

**Kuwerenga**
1 Yohane 5.12-15

**Malongosoledwe**
Yesu anauza ophunzira ake kuti Atate adzatipatsa zabwino zonse zimene timpempha. Ndipo adzatithandiza ndithu kukhala abwino ngati timpempha.
Yesu anauza ophunzira ake nthano yaing'ono. Anati, 'Yerekezani kuti mnzanu abwera kukuonani usiku. Acoka kutali ndipo ali ndi njala. Mufuna kumpatsa cakudya koma mulibe buledi m'nyumba. Ndipo pa nthawi ya usiku masitolo onse ndi obvalika. Ngati ciri tero, mudzapita ku nyumba ya mnzanu wina kumpempha buledi. Mudzagogoda pa citseko. Mnzanu auka. Mumuitana, 'Anzanga, mungandipatse buledi kodi? Ndiri ndi mlendo wakumva njala ndipo ndiribe cakudya.' Kodi mnzanu adzayankha ciani? Kodi adzalankhula tero, 'O, osandibvutitsa, ife tonse tigona ndipo sindifuna kuuka kukakupatsani buledi'? Iai, sadzalankhula tero. Ngati iye ndi mnzanu ndithu, iye adzauka kukakupatsani mabuledi onse omwe mufuna.'
Yesu anauza ophunzira ake kuti kotero ndi m'mene Mulungu aliri. Mulungu sadzanena konse, 'Osandibvutitsa'. Sadzanena 'iai' pamene timpempha cimene tisowa. Mulungu ndi Mnzathu wabwino kwambiri. Osati Mnzathu cabe: Iye ndi Atate wathu wa Kumwamba ndipo atikonda. Adzatipatsadi zabwino zimene timpempha.
Atate wathu wa Kumwamba adziwa kuti sitikwaniritsa kukhala konse abwino. Adziwa kuti kukhala moyenera miyoyo yathu kwa Iye ndiko cinthu cobvuta kwa ife. Adziwa kuti ndife ofooka ndi ocimwa. Koma afuna kuti tizikhala miyoyo yathu kwa Iye. Ndipo akondwera potithandiza kucotsa comera cosafunika ca macimo m'mitima yathu.
Poyamba tiyenera kumuuza za mbeu zonse zosafunika za macimo ndiponso momwe ziliri. Kenaka tiyenera kumupempha kutithandiza. Tiyenera kumpempha kutisandutsa kotero kuti tifuna kucotsa comera conse cosafunika. Tiyenera kumpempha kutisandutsa kukhala oima nji kucita zoyenera.
Tiyenera kumpempha kutisandutsa kukhala oima nji kunena 'iai' pa zoipa zonse.
Tiyenera kumpempha kudzala mitima yathu ndi cikondi. Ngati timkonda kwambirimbiri, kukhala abwino si bvuto lalikulu.
Tiyenera kumpempha Mzimu Woyera kukhala m'mitima yathu ndi kutitsogolera m'njira yabwino, kutisandutsa kuti tikhala amphamvu kukhala miyoyo yathu kwa Atate wa Kumwamba ndi kwa Yesu.
Mulungu adzatipatsa izi zonse pamene timpempha, pakuti analonjeza kutipatsa ciriconse cimene citipindulitsa. Koma tiyenera kufunadi kukhala abwino.

**Kukambirana**
1. Fotokozani njira momwe Mulungu ndi Atate wabwino.
2. Kodi Mulungu Atate atipatsa zonse zomwe timpempha?
3. Kodi tiyenera kupempha ciani Mulungu Atate?
4. Kodi mufuna kuti Mulungu Atate akupatsani zabwino za uzimu zotani?
5. Fotokozani cifukwa ciani timapempha Mulungu Atate m'dzina la Yesu.

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Tikuyamikani kuti ndinu Atate wabwino. Mudziwa zimene ziri zitipindulitsa m'miyoyo yathu ya uzimu ndi ya pa dziko lapansi. Tikupemphani kuti muticitire zabwino mwa cisomo mwa Yesu Kristu Mpulumutsi. M'dzina la Yesu tikupemphani, Amen.

## 8. Mzimu Woyera atithandiza

*Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro – Agalatiya 5.22*

**Kuwerenga**
Yohane 15.1-5

**Malongosoledwe**
Yesu ananena kuti adzakhala ndi ife. Anatumanso Mzimu Woyera kukhala mwa ife.
Makamaka Mulungu Mzimu Woyera atithandiza kukhala abwino. Mzimu Woyera atiuza kucita ciani.
Paulo mtumiki anapita ku mizinda yambiri kuuza nthano ya Yesu. Anapitanso ku Galatiya. Ndipo anthu ambiri a ku Galatiya anakhulupirira Uthenga Wabwino. Anasanduka Akristu. Indedi, kucokera ku nthawi iyo, iwo anafuna kukhala miyoyo yao kwa Mulungu.
Koma patapita nthawi pamene Paulo sanali nao, anthu a ku Galatiya anayamba kubvutana. Anaiwala kukhala momwe ana a Mulungu ayenera kukhala. Sanakondane moyenera. Anthu ena anadzikonda ndipo ena anamva nsanje.
Paulo anamva za izi. Anamva cisoni kuti iwo sanacite bwino. Anawalembera kalata. Tikhoza kuwerenga kalata ilo. Lipezeka m'Baibulo: kalata la Paulo mtumiki lolembedwa kwa Agalatiya.
Mu kalata ilo Paulo anauza Agalatiya kuti saloledwa kubvutana ndiponso kuti ayenera kuleka kudzikonda ndi kumva nsanje. Anawauza momwe Mulungu adzawathandiza.
Paulo anawalembera, Ngati muyendayenda mwa Mzimu, musacita zinthu izo. Ngati muyendayenda mwa Mzimu, mudzaonetsa zipatso za Mzimu.
Kodi Paulo anatanthauza ciani?
Cabwino, mudziwa kuti mtengo wabwino wa apozi udzabala maapozi abwino. Ndipo mtengo wabwino wa mango udzabala mango zabwino. Zipatso zathu zabwino ndizo zinthu zabwino zocokera m'mitima yathu: cikondi, kukoma mtima, coonadi, cimwemwe ndi zabwino zina zonse. Ndipo tikhoza kukhala ndi zipatso izo zabwino ngati Mzimu Woyera akhala m'mitima yathu. Iye akhala m'mtima wa munthu aliyense wokonda Yesu, monga mudziwa.
Koma nthawi zina tiribe zipatso zotere. Nthawi zina ana a Mulungu abereka zipatso zoipa (monga kukalipa, nsanje, kuda) monga mtengo woipa ndiponso monga Agalatiya anacita. Tsono, Paulo ananena, ngati mungomvera Mzimu Woyera ndi kucita zimene Iye akuuzani, mudzabala zipatso zabwino m'malo mwa zipatso zoipa. Ici ndi cimene Paulo anatanthauza pamene anauza Agalatiya kuyendayenda mwa Mzimu.
Sitikwaniritsa konse kukhala miyoyo yathu kwa Mulungu ngati Mzimu Woyera satithandiza. Iye atisandutsa kukhala ofuna kukhala abwino. Iye atiuza momwe tizikhala abwino. Atiuza mu Baibulo, Mau a Mulungu. Pamene tiwerenga Baibulo, Iye atithandiza kumvetsa citanthauzo cake ndi momwe tizikhala miyoyo yathu.

**Kukambirana**
1. Kodi mwacita coipa cotani lero?
2. Mulungu akamba kuti, 'Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse' (1 Yohane 1.9). Kodi tiyenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi kuti tipeze cipulumutso?
3. Kodi Mzimu Woyera amacita ciani?
4. Cifukwa ciani tifunika Mzimu Woyera?

**Citsanzo ca pemphero**
Tikulemekezani, Mulungu wamkulu, kuti ana anu alandira zonse kuti akhale abwino pa maso panu. Osati cikhululukiro cabe komanso ciyeretso. Tipatseni Mzimu Woyera kutiphunzitsa momwe tikhala pa maso panu komanso kuti timvetsetsa Baibulo kuti tikhala miyoyo yathu kwa ulemerero wanu. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu, Amen.

## 9. Yesu atipempherera

Ambuye Yesu anati kwa Atate wake:

*Ine ndiwapempherera iwo; sindipempherera dziko lapansi, koma iwo amene mwandipatsa Ine, cifukwa ali anu: ndipo zanga zonse ziri zanu, ndi zanu ziri zanga; ndipo ndilemekezedwa mwa iwo – Yohane 17.9 ndi 10*

**Kuwerenga**
Yohane 17.9-15

**Malongosoledwe**
Mulungu Atate atithandiza kukhala miyoyo yathu kwa Iye ngati timpempha. Mzimu Woyera atithandiza pamene tiyendayenda mwa Mzimu. Ndipo Yesu, Mwana wa Mulungu, atithandizanso. Yesu atipempherera. Apempherera ana ake onse.
Sitikhoza kuona Yesu. Iye ali Kumwamba. Koma ationa. Ayang'ana pansi. Aona zonse zimene ticita. Ayang'ana tsopano lino m'mitima yathu. Amakhala m'mitima yathu. Adziwa pamene timkonda ndiponso pamene tifuna kukhala abwino.
Ndipo atipempherera. Apempha Mulungu Atate kutisunga kutali kwa uchimo.
Tsiku lina pamene Yesu anali pa dziko lapansi, Iye anati kwa Petro, 'Satana afuna kukhala ndi iwe. Adzayesa kukutenga. Koma ndinakupempherera.'
Yesu anapempherera Petro pakuti sanafune Satana kutenga Petro. Yesu anakonda Petro.
Petro anacimwira Yesu. Anakana Yesu. Anaopa ndipo ananena kuti sadziwa konse Yesu.
Ici cinacititsa cisoni Yesu.
Koma atacimwa, Petro anamva cisoni. Anamva cisoni kwambiri kotero kuti analira. Ndipo Yesu anakhululukira Petro. Petro anakhalabe m'modzi wa Yesu. Satana sanamtenge angakhale anampangitsa Petro kucimwira Yesu.
Kucokera pa nthawi iyo, Petro anakonda Yesu kuposa momwe adamkonda kale. Anakhala wakuyamika kuti Yesu adampempherera. Anakhala wakuyamika kuti Satana sanamtenge.
Yesu asanapite Kumwamba, analankhula ndi ophunzira ake nthawi yaitali. Anawauza kuti adzapita Kumwamba kuwakonzekera malo. Ndipo kenaka anapemphera ndi iwo. Komanso anawapempherera. Ndipo anatipempherera.
Ngakhale tsopano Iye atipempherera. Ganiziraniko: Yesu Kumwamba aona ife pansi ndipo atipempherera. Angodziwa zimene tisowa. Angodziwa pamene tiyesedwa kucita coipa. Adziwa momwe tiyesa kucita zinthu zoyenera. Ationa pamene ticimwa. Apempha Atate wake kutisunga kutali kwa macimo, kutiyeretsa ndi kutipangitsa kukhala okondana.

**Kukambirana**
1. Kodi Ambuye Yesu ali kuti?
2. Kodi Ambuye Yesu amacita ciani?
3. Kodi Ambuye Yesu athandiza bwanji ana ake kuti akhala miyoyo yao kwa Mulungu?
4. Ana a Mulungu apulumutsidwa mwa cisomo. Fotokozani cifukwa ciani nchito zathu zabwino sizikhoza kutipulumutsa. Nanga inu, mwapulumutsidwanso mwa cisomo?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu Kristu, Zikomo kwambiri kaamba ka mapemphero anu. Tikupemphani kuti mutisunge kutali kwa macimo. Mutilimbikitse kuti tidzakhala miyoyo yathu ku ulemerero wanu, kuti tikumverani nthawi zonse. Tidziwa kuti sitiyenera konse cisomo canu, ndiye tikupemphani m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.

## 10. Angelo atilondera

*Pakuti adzalamulira angelo ace za iwe, akusunge m'njira zako zonse – Salimo 91.11*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 12.5-11

**Malongosoledwe**
Simunaone konse mngelo. Ndipo ine sindinaone konse mngelo.
Angelo ndiwo mizimu. Sitikhoza kuona mizimu.
Kale kwambiri pamene Mulungu anali ndi uthenga wapadera, nthawi zina Iye anatuma mngelo pansi pa dziko lapansi kuuza uthengawo.
Mukumbukira momwe mngelo anadza kuuza abusa kuti Yesu abadwa. Ndipo kenaka abusa anaona makamu a angelo oimba ku thambo. Kunali angelo ambirimbiri.
Angelo ndiwo othandiza a Mulungu. Ndiwo atumiki ake. Baibulo litiuza kuti nthawi zina Mulungu atumabe angelo kuthandiza anthu ake, ngakhale sitiwaona konse.
Kale kwambiri pamene Mulungu anabweretsa anthu ake Aisrayeli kucoka m'Aigupto, Iye anatuma mngelo kuwatsogolera. Anapanga thambo lalikulu limene anthu onse anakhoza kuona. Mngelo anali m'thambo. Pamene mngelo anayendetsa thambo, anthu analondola. Pamene mngelo anaimiritsa thambo, anthu anapuma.
Tsiku lina mfumu wa Aigupto ndi asirikali ake onse anapitikitsa anthu a Israyeli. Mfumu Farao anafuna kuwasandutsanso akapolo ake. Pa nthawi iyo mngelo anayendetsa thambo kupita kumbuyo kwa Aisrayeli. Thambo linali pakati pa Aisrayeli ndi Aaigupto, kuti Aaigupto sangapweteke Aisrayeli.
Angelo amacita zodabwitsa zambiri. Mngelo anacotsa mwala ku manda kwa Yesu, Iye atauka kwa akufa. Kotero anzake a Yesu anakhoza kuona kuti manda unali wopanda kanthu. Ena a azimai amene anabwera ku manda, anaona mngelo ndipo iye anawauza kuti Yesu anali wamoyo.
Pa nthawi ina Petro anaikidwa m'ndende cifukwa analalikira za Yesu. Abwenzi a Petro anaganiza kuti sadzamuonanso konse. Anampempherera. Usiku uja pamene Petro anali gone, iye anamva wina kudza mbali ya thupi lake. Anatsegula maso ake ndipo anaona mngelo! Mngelo anapasula nsinga za pa manja ake. Ndipo anamtsegulira Petro citseko ca ndende. Asirikali omyang'anira sanamve ngakhale Petro kutuluka. Ndipo abwenzi a Petro anakondwera kwambiri pamene Petro anadza kwa iwo.
Nthawi ina Yesu anauza ophunzira ake kuti kuli angelo apadera olondolera ana a Mulungu. Ici ndi cinthu codabwitsa, iai? Atate wa Kumwamba anauza angelowa momwe ayenera kusamalira ana a Mulungu.
Pamene tiganizirako zonse zimene Mulungu acita kutithandiza, ngakhale kutuma angelo kutilondolera, ndife akuyamika kwambiri! Ndipo tifuna kwambiri kukhala miyoyo yathu kwa Mulungu ndi kumsangalatsa. Ngati tiyesa kumkondweretsa, ndife okondwera kwambiri.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani sitikhoza kuona angelo?
2. Kodi nchito ya angelo ndi yotani?
3. Kodi angelo amamvera yani?
4. Nanga inu, mumamvera yani? Mulungu kapena zilakolako zanu?

**Citsanzo ca pemphero**
Atate wathu wa Kumwamba, Sitikhoza kuona angelo koma tidziwa kuti aliko. Tikuyamikani kuti muwagwiritsa nchito kucita cifuniro canu. Tiphunzitseni kukumverani monga iwo amakumverani moonadi. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu, Amen.

## Sewero

Pezani mau awa onse

| | | | |
|---|---|---|---|
| Mulungu | cisamaliro | pemphero | moyo |
| thandizo | kukondwa | Yosefe | Kristu |
| angelo | Yesu | mbeu | onse |
| Danieli | Atate | mzimu | |

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| E | M | C | I | S | A | M | A | l | I | R | O |
| T | U | M | O | Y | O | Z | L | A | E | D | Z |
| A | L | S | U | T | S | I | R | K | F | A | I |
| T | U | O | N | S | E | M | A | V | E | N | D |
| A | N | G | E | L | O | U | Z | B | S | I | N |
| J | G | P | E | M | P | H | E | R | O | E | A |
| D | U | S | E | Y | M | B | E | U | Y | L | H |
| K | U | K | O | N | D | W | A | B | P | I | T |

**Nyimbo**

Poyenda ndi Mbuye, mkuwala kwaceko,
Aunikira m'njira mwathu;
Pakugwira nchito amakhala nafe,
Khulupira ndi kumeratu.

*Khulupira, palibenso njira,*
*Yakukondwa mwa Yesu,*
*Komatu kumvera.*

Mthunzi sungagwetu, pena mtambo bwera,
Komatu azipirikitsa;
Nkhawa ndi cisoni zidzacoka msanga
ngati, tikhulupira Yesu.

'Fukwa ca ntchitoyi ndi zisoni zathu,
Adzatidalitsa mokwana;
Kopandanso imfa kapena kukwiya,
Tidzadalitsika pomvera.

Sitingadziwetu za cikondi cace,
Mpaka titadziperekatu;
'Fukwa cifundoco ndi cimwemwe cace
Amapatsa anthu omvera.

Pompo m'ciyanjano tidzakhala naye,
'Pena yendamo m'njira yace;
Ndipo tidzacita cifuniro cace,
Tidzakhala omvera ndithu.